


TCHIMO, UTHENGA WABWINO, NDI MALAMULO






“Ine sindidzaiwala konse malangizo anu, pakuti ndi malangizo anuwo munasunga moyo wanga. Ndine wanu, ndipulumutseni; pakuti ndasamala malangizo anu”

(Masalimo 119:93, 94, ccl)

Padziko lino, uchimo ndi vuto lomwe limakhudza ife tonse, ndikuwononga ubale wathu ndi Mulungu: “pakuti onse anachimwa, naperewera pa ulemelero wa Mulungu. (Aroma 3:23).

Kodi tingakonze bwanji kusagwirizana kumene uchimo umabweretsa pakati pa Mulungu ndi ife? Pali maganizo awiri omwe angathetse vutoli: Malamulo okha (kupulumutsidwa malingana ndi ntchito zathu, lomwe liri lingaliro lolakwika la ntchito ya Lamulo); kapena Uthenga Wabwino okha (chipulumutso mwa chikhulupiriro kuchotsapo Lamulo)

Tikufunika kudziwa kuti Lamulo ndi Uthenga Wabwino zimagwirizana munkhondo yathu yolimbana ndi uchimo. Chirichonse chiri ndi ntchito yake.



- 👉 Kupewa mayesero
- 👉 Malangizo opewera tchimo

TCHIMO



📖 Lamulo ndi tchimo

LAMULO



- ✝️ Uthenga Wabwino ndi Malamulo
- ✝️ Kumangidwa pa thanthwe

UTHENGA WABWINO



III TCHIMO




KUPEWA MAYESERO

“koma munthu aliyense amayesedwa akakokedwa ndi zilakolako zake zoyipa ndi kukopedwa nazo.” (Yakobo 1:14 CCL)




Yakobo amati munthu okana mayesero ndi odala. (Yakobo 1:12). Akupitiriza kufotokoza kuti mayesero sachokera kwa Mulungu (Yakobo 1:13), koma amachokera ku zilakolako zathu zoipa (Yakobo 1:14)

Paulo ananena za “woyesa” (1 Atesa 3:5) amene Yesu anamutcha Satana (Mateyu 4:3,10). Iye amadziwa bwino kugwiritsa ntchito zofooka zathu kuti atitsogolere ku uchimo. Tisaiwale za nkondo yapakati pa Khristu ndi Satana, ndikuti woyesa amafuna kuti atichotse kwa Khristu. Timutsate iye.



Samson ndi chitsanzo chabwino kwambiri cha muthu amene amagonja pamayesero potsata maganizo ake, ngakhale akudziwa kuti akuchita zosemphana ndichifuniro cha Mulungu. (Oweruza 14:1-3; 16:1,4)

Tingapewe bwanji mayesero? Tichite chifuniro cha Mulungu (Mateyu 6:33); kupeza nthawi yolankhulana naye (Mark 14:38); kutenga chishango cha chikhulupiriro (Aefeso 6:16)



MALANGIZO OPEWERA TCHIMO

“Ndipo ngati diso lako likuchimwitsa, likolowole. Ndi kwabwino kwa iwe kulowa ufumu wa Mulungu ndi diso limodzi, kusiyana ndi kukhala ndi maso awiri ndi kuponyedwa ku gehena” (Marko 9:47)

Yesu anatisiyira malangizo omveka bwino kuti tipewe uchimo:



Pewani kuchita zinthu zomwe zingakupangitseni kuchimwa (Marko 9:43; Yobu 23:12).

Mwachitsanzo, kugula mowa.

Pewani kupita kumalo koti mukachimwa (Marko 9:45; Yobu 23:11). Mwachitsanzo, kupita ku malo azisangalalo usiku

Pewani kuyang'ana zinthu zomwe zingakuchimwitseni ngati kuonera mafilimu azolaula (Marko 9:47; Yobu 31:1)



Mwachidule, tiyesetse kupewa kuchimwa komanso kuyesedwa kuti tichimwe. Osaiwala kupemphera


- 1 Musaganize kuti ndinu okwanira mungachite zinthu panokha (1 Akorinto 10:12)
- 2 Lekani kudzitamandira zaubwino wanu, khalani odzichepetsa ngati Yesu (Mateyu 6:2)
- 3 Ziphunzitseni kuchotsa zilakolako mumtima mwanu (Mateyu 5:28-29)
- 4 Lekani kunyogodola ndi kuweruza ena (1 Akorinto 4:5)
- 5 Pemphererani adani anu. Mupewe kukhala ndi adani (Mateyu 5:44)
- 6 Lekani kukwiwira anthu amene mumakhala nawo (Mateyu 5:22)



LAMULO III


LAMULO NDI TCHIMO

"Aliyense amene amachimwa amaphwanya lamulo; pakuti tchimo ndi kuphwanya lamulo." (1 Yohane 3:4)



Ubale wa Malamulo ndi uchimo watanthauziridwa molakwika ndi anthu amene amati kusunga lamulo kungathe kuwaombola ku machimo awo (Agalatiya 5:4). Kaganizidwe kameneka kapangitsa ena kumanena kuti Malamulo anathetsedwa.


Vuto ndiloti ena amaona ngati pali ubale pakati pa Malamulo ndi chipulumutso, kuti lamulo ndilolepheretsa kapena ndi njira yokhayo yachipulumutso. Koma ntchito ya Lamulo sinakhalepo yopulumutsa. Nanga ntchito yake ndi yotani?




Lamulo limationetsa tchimo (1 Yohane 3:4). Popanda Lamulo sitikanadziwa kuti tchimo ndi chiyani (Aroma 7:7), ndipo chifukwa chake sitikanafunafuna yankho lake (Agalatiya 3:24).

Lamulo ndi mpanda otiteteza kuti tisavutike ndi zotsatira za uchimo (1 Yohane 5:3; Masalimo 1:1-3)





UTHENGA WABWINO




UTHENGA WABWINO NDI MALAMULO

"Pakuti timanena kuti munthu ayesedwa olungama ndi chikhulupiriro, popanda ntchito za lamulo (Aroma 3:28)

Chipulumutso chathu (chikhululukiro cha machimo ndi moyo wosatha) chikupezeka mu msembe ya Yesu pamtanda (Agalatiya 3:13). Yesu ndiye chitsanzo chathu (1 Yohane 4:9,19). Timaonetsa chikondi chathu pakusunga malamulo ake (Yohane 14:15)

Tiunike ubale wapakati pa Malamulo ndi Uthenga Wabwino (ndiko kuti, chipulumutso kudzera munsembe ya Yesu):



Yesu sanathetse Lamulo koma kutsindikiza (Mateyu 5:17). Lamulo ndi Uthenga Wabwino ndi chithunzithunzi cha khalidwe lenileni la Mulungu: Chikondi.



ANAMANGA PA THANTHWE

"Ndichifukwa chake aliyense amene amva mau anga ndi kuwachita akufanana ndi munthu wanzere amene anamanga nyumba yake pa thanthwe." (Mateyu 7:24)



Kulandira Uthenga Wabwino kulinso ndi njira zofunika kutsatira. Choyamba ndi chidziwitso. Tiyenera kudziwa kuti pali otiombola (Aroma 10:14).

Koma chidziwitso chokha sichingatipulumutse. Yesu anayerekezera anthu amene amalandira chidziwitso cha chipulumutso koma osagwiritsa ntchito mfundo za uthenga wabwino m'miyoyo yawo ndi munthu amene anamanga nyumba yake pa mchenga, ndipo 'kugwa kwake kunali kwakukulu' (Mateyu 7:26-27)



**Chidziwitso ndi zochita ziziyendera limodzi (Mateyu 7:24-25)
Timalungamitsidwa popanda ntchito za lamulo (Aroma 3:28),
koma ntchito zathu zionekere kuti tikuchita chifuniro cha Mulungu
ngati anthu opulumutsidwa (Mateyu 7:18-21)**

Tikalandira Yesu kukhala bwenzi lathu lapamtima, kusunga malamulo ake, timamanga pa thanthwe.



“Lamulo limaulula machimo a munthu, koma silipereka thandizo. Limalonjeza kuti limapereka moyo kwa olimvera ndi onyozera adzafa ndithu. Uthenga Wabwino wa Khristu okha ungapulumutse ku chilango kapena kuipitsidwa ndi uchimo. Munthu ayenera kulapa kwa Mulungu ndipo chikhulukiro chimachokera kwa Khristu yemwe ndi nsembe yosachimwa. Chotero tikakhulukidwa timakhala oyenera chipulumutso”

EGW (The Great Controversy, p. 467)